COVID-19: Nthawi zonse satilani uphungu wa boma komanso acitetezo za umoyo.

Umoyo

Nkhani 10
hello@dignityonline.org.uk
+447340 573 937

Kupasa Mofikapo

Mtumwi Paulo, osatila wa Yesu ofikapo, anayamba kacisi ku Makedonia. Kunali kachisi wa anthu anali 'mu umphawi'. Saliokha. Ali ambili osauka anthu omwe asatila Yesu kwa zaka zikwi zikwi. Aku Makedonia anakumana ndi mabvuto ambili ndipo sanali opata ndalama. Ndipo analinso odalilika kwambili. Mwa 2 Akolinto 8:1-7 tiwerenga zaiwo ndi mbili yao ya mphamvu.

Aku Makedonia anali odalilika kupambana monga anayembekezeledwa kukhalila. Sana ngo pasa chabe zomwe anali nazo mco sungila kapena kuti cinali chapafupi kwa iwo. Kumbukilani kuti anali amphawi othelatu ndi anthu ambili kubvutika. Koma analakalaka kupasa. Nchifukwa cache Paulo awa gwiritsa nchito monga chisanzo chopasa. Izi ndizo Paulo ananena zaiwo: "Ndichitila umboni kuti anapasa zoculuka monga anakwantsila, ngakhalenso kupitilila pamuyeso wao. Mozipeleka okha, mofulumila anatipapatila ife chifukwa cha danga lopasa motumikila anthu a Ambuye."

Chikuoneka ngati malingalilo obodyoka! Chilli monga anena, 'Ndife aumphawi ndipo tilibe zocuuluka telo tiyeni tipase bena.' Nichifukwa ninji anachita telo? Ndime inena kuti, "chimwe mwe ndi umphawi wao ochuluka zisonkhanisidwa kukhala chuma chachilungamo". Anali ndi chikhulupililo ndi kudalila mwa Mulungu comwe china apangisa iwo kukhala ndi chikondi pa bena kuti anapasa moyenera kuchokera mu umphawi wao. Ana werengera ena kukhala ofunikila ndiponso oyenera ndalama zao kopambana iwo okha. Nanga tichita izi kangati?

Coonadi chokongola muuthenga uyu ndi waife, kulibe kanthu olemela kapena osauka, tiyenela kutamanda Mulungu pamodzi moyenera. Uthengau siwa munthu umodzi kupasa, chidalila bungwe lonse la okhulupilila kupasa pamodzi. Nthawi zonse nichobvuta kuchita zinthu mwaife tokha. Ngati muganiza, 'Nanga nsonga yaine kupeleka pomwe ndipeleka chabe kang'ono?' Pamodzi tingachite zazikulu. Tingaike mphanso zathu pamodzi ndi mphanso zaena kupambana kamtengo kang'ono kamakhala kakulu. Iyi ndiyo mphamvu ya mabungwee odalilika. Ndichapa fupi kuyanganila pa mabvuto athu, muli monse momwe zilili, ndiku gamula kuti tingathe kapena iyayi kupasa ena. Ninga limbikise tonse kukhala wodalilika kwa ena pamodzi, monga kachisi kaku Makedonia?

Ziyikeni mu Zocita!

Chikulu pa kudalilika ndichakuti tingayambile pomwe tilili! Ndi bungwe lanu, kapena bungwe la anzathu, kugamula kupasa monga aku mpingo waku Makedonia anthu osaukilatu kuposa inu. Nichifukwa ninji simunga sonkhanise khobidi, zakudya, kapena zinazache za ao osowekere m'mdzi wanu kapena mdzinda? Mungathe kupereka zobvala, nthawi, mwina zilizonse, malinga ngati munazilipilila ndipo mwazipereka modaliladi. Chili chonse mufuna kupasa chizakhala thandizo lalikulu.

Pephelani kuti:

1) Mulungu azatenga mphaso yomwe upasa ndiku ichulukitsa ndiku dalisa olandila.
2) Pomwe upasa uzadabwa ulandila chimwemwe cochuluka!

Wopempheresa Esau* mosachedwapa anapeze kopo pa msonkhano wa maphunziro a Bungwe Lamoyo. Ndipo anasisimutsidwa ndizomwe anamva ndikupeleka N5120 ($8) kwa awo osogolela maphunziro. Wopempheresa Esau anakasewenzesa nkobidi iyi kupata zofuna za ena, koma aganiza zo kutukula nchito ndi kudalisa ena ophunzila za Mabungwe Yamoyo, omemezedwa m'mdzinda.

- Wopempheresa Esau,*Yinsu, Namibia.



Phunziloi yasisimutsidwa ndi "Pasa monga Kachisi kaku Makedonia" phunzilo yo Konda Mdzi Wanu. Mngafufuze zochuluka pa: **dignityonline.org.uk/publications**

Dignity ndi bungwe ya zaulele yosindikizidwa pa No. 1122656. Dignity (Worldwide) ndi kampani yoziyimilila pa yokha, yosindikizidwa ku England ndi Walesi No. 6394480. Dignity Zambia Limited ndi kampani yomwe anthu aphindulako yosindikizidwa mu ziko la Zambia pa No. 117117

*dzina lisinthidwa ku lamwine

Chewa